# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA BALAKA M'DZINJA LA 2024 -2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE


Nyengo ya mvula ya 2024-2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira koposa mlingo kwa madzi pakati cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.
Boma la Balaka likuyembekezeka kulandira mvula yochulukirapo kuyerekeza ndi chaka chatha ndipo ikhala ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo.

## October 2024




Boma la Balaka likuyembekezereka kudzalandira mvula yochepa kwambiri mu mwezi wa October. Mlingo omwe ukuyembekezereka ndi osaposera 30mm. Chifukwa cha kutentha, mvula imeneyi ikhoza kudzakhala ya mabingu ndi mphepo yamkuntho.


## November 2024




Mu mwezi wa November, boma la Balaka lidzalandira mlingo wosaposera 70mm. Ndipo mvula imeneyi ikhoza kudzagwa ndi mphepo ya mkuntho komanso mabingu.

Madera ambili a m'bomali, Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzayamba mu sabata lachitatu la mwezi wa November kufikira sabata la chiwiri la mwezi wa December 2024.


## December 2024




Mvula ya mlingo oposa 150mm ikuyembekezereka mu mwezi wa December m'boma la Balaka. Mlingo uwu ndi wapakati kati wa boma la Balaka.


Nyengo yadzinja m'madera ena ochepa ikuyembekereka kudzayamba mochedwa mu sabata lomaliza la mwezi wa December.

## January 2025





Mvula ikuyembekezereka kudzagwa yochuluka mu mwezi wa January. Madera ozungulira TA Nsamala akuyembekezereka kudzalandira mlingo wosaposa 200mm. Koma madera ambiri adzalandira mlingo woposa 300mm maka madera ozungulira TA Kalembo.
Chiopsezo cha ng'amba yapafupifupi sabata ndichokwera mu mwezi wa January.

## February 2025




Mlingo wa pakati pa 150 200mm ukuyembekezereka m'madera ambiri aku Balaka mu mwezi wa February. Uwu ndi mlingo woposa mlingo okhazikika m'madera ambiri. Madera ozungulira TA Kalembo ndi Balaka town adzalandira mlingo oposa 250mm.
Ng'amba yapafupifupi masiku 7 ikuyembekezereka m'bomali mu mwezi wa February.


## March 2025




Mu mwezi wa March mlingo wa mvula omwe ukuyembekezereka ndi wa pakati pa 100 komanso 150 mm.

M'madera ena abomali, nyengo yadzinja ikuyembekezereka kudzafika kumapeto mu sabata lachitatu la mweziwu.

## April 2025





Pomwe nyengo yadzinja idzakhale ikupita kumapeto, madera ambiri a boma la Balaka adzalandira mulingo wa pakati pa 50 ndi 100mm.

Nyengo ya dzinja m'madera ena idzatha kumapeto kwa mwezi April.

*Mvula yodzalila ikuyembekezeleka pakati pa sabata yachitatu ya November ndi sabata yoyamba ya mwezi wa December 2024. Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzatha pakati pa sabata yachitatu ndi sabata yachinayi ya mwezi wa April 2025. Ng'amba yamasiku woposera asanu ndi awiri ikuyembekezeleka m'mwezi wa January komanso wa February m'chaka cha 2025. Kutalika kwa nyengo yadzinja kukuyembekezeleka kukhala kwa masiku a pakati pa 105 ndi 126.*
*Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ya pamwezi yaperekedwa m'munsimu.*

| BALAKA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 1.2 | 16.4 | 9.8 |
| NOV | 42.9 | 86.5 | 34.1 |
| DEC | 112.1 | 178.6 | 140.1 |
| JAN | 212.3 | 291.4 | 302.0 |
| FEB | 115.5 | 174.5 | 244.2 |
| MAR | 78.3 | 134.7 | 115.8 |
| APR | 7.2 | 32.9 | 29.5 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**

The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

© Poster Template by Genigraphics® 1.800.790.4001 www.genigraphics.com